



United Nations
Educational, Scientific and
Cultural Organization



Atsogoleri A Ndale:

DEWANI ZAMBIRI ZOKHUDZA UBEREKI NDI ZOGONANA PAKATI
PA ACHINYAMATA KOMANSO THANDIZO LOMWE ANGAPEZE!

Tsogolo labwino, Umoyo wa bwino wa Achinyamata!

A tsogoleri andale amakhala otekeseka ndi zinthu zomwe anthu awo akukumana nazo. Maphunziro oyenera komanso okwanira okhudzana ndi za umunthu, kugonana komanso ubereki pakati pa achinyamata ayenera kuperedwa potengera chikhalidwe komanso msinkhu wa achinyamata omwe tikufuna kuwampunsitsa kapena kulangiza.

Kafukufuku akuonetsa poyera kuti kuphunzitsa kapena kupereka uphungu wokhudzana ndi zomwe zimachitika ndi kuoneka pamatupi a achinyamata akamakula, komanso nkhani zokhudza kugonana zimathandiza kuti achinyamata apewe mchitidwe okhala ndi zibwezi zambiri zogonana nazo, amadziwa njira zolelera, zam'mene angapewere HIV ndi matenda ena opatsirana pogonana komanso mimba zosayembekezera.

Thandizani pa nkhani zokhudzana ndi ubereki ndi zogonana pakati pa Achinyamata: Thandizani Atsogoleri a mawa!

Kodi chifukwa chiani nkhani zokhudzana ndi ubereki ndi kugonana pakati pa achinyamata ziyenera kukhala ndi malo akeake apadera oti achinyamata azipita kukalandilako mauthenga, zida ndi zipangizo zina zofunika?

Maphunziro, mauthenga, zida zoti achinyamata atha kugwiritsa ntchito zokhudzana ndi umunthi, kugonana ndi ubereki ziyenera kuti zizipezeka mosavuta, zikhale zotsika mtengo komanso zodalirika kuti achinyamata athe kuzipeza ndi kugwiritsa ntchito.

Pali chiopsyezo pakati pa achinyamata komanso vuto lalikulu kumadera kumene kumakhala achinyamata ngati zida munga makondomu, njira zolerera, mankhwala munga ma ARV komanso mankhwala ena ochiza matenda ena opatsirana pogonana, komanso othandiza atsikana amene ali ndi mimba azipezeka mosavuta. Ichi ndi chifukwa chake maphunziro, mauthenga ndi zida zoterezi ziyenera kumapezeka mma'sukulu, ndi malo ena apaderadera kumidzi ngati njira imodzi yothetseratu vutoli kuno kum'mawa ndi kumwera kwa Africa.

Kodi tikamati kupereka maphunziro, mauthenga, ndi zida mwapaderadera zoti achinyamata athe kugwiritsa ntchito zokhudzana ndi umuntui, kugonana ndi ubereki zimatanthauza chiani?

Uku ndi kupereka maphunziro, mauthenga, zida zoti achinyamata atha kugwiritsa ntchito zokhudzana ndi umunthu, kugonana ndi ubereki mosavuta ndi mwa chinsinsi moti achinyamata atha kupitako ndi kuthandizika malingana ndi zomwe akufuna. Izi ziyenera kutero potengera umoyo wao okhudzana ndi kugonana ndi ubereki, ufulu wao wachibadwidwe komanso zina ndizina. Izi makamaka zimakhudza uphungu wa:

- Za umoyo.
- Zibwezi ndi zogonana.
- Nkhanza
- Njira zolelera
- Njira zopewera matenda opatsirana pogonana kuphatikizirapo HIV.
- Zochotsa mimba yosayembekezera potengera malamula adziko lino.
- Zauchembere makamaka atsikana akatenga mimba komanso akabereka.

Maphunziro oyenera komanso okwanira okhudzana ndi za umunthu, kugonana ndi ubereki ndi amene amaperekedwa kwa achinyamata panthawi yoyenera ndipo amapangitsa achinyamata kukhala odzidalira, otha kupanga zisankho pamoyo wao watsikunditsiku okhudza zogonana, komanso kudziletsa pankhani zogonana.

“Palibe chikhulupiliro chachikulu chimene dziko lonse la pansi chili nacho kuposa chikhulupiliro mwa ana Palibe udindo waukulu umene dziko lonse la pansi uli nawo kuposa undindo oyang'anira ana ndi kuonetsetsa kuti ufulu wa wachibadwidwe sukuponderezedwa, zofuna zao zikupezeka nd kukwaniritsidwa komanso kuti alibe nkhwana ndipo kuti akukhala moyo wabwino ndipo kuti zofuna zao zikukwanilitsidwa.”

– Kofi A. Annan, Aliyekuwa Katibu Mkuu wa Umoja wa Mataifal

Chifukwa chiani atsogoleri a ndale ayenera kumatenanga nawo mbali?

Kum'mawa ndi kumwera kwa Africa achinyamata 52 mwa achinyamata 100 aliwonse amatenga kachilombo koyambtsa matenda a Edzi ka HIV. Ndipo mwa achinyamata 100 omwe amatenga kachilomboka, 60 ndi atsikana kusonyeza kuti matenda a Edzi akukhudza achinyamata kwambiri makamaka atsikana. Izi zikusonyeza kuti ndikofunika kuti atsikana athandizidwe ndi kuphunzitsidwa bwino za ufulu wao wachibadiwdwe ndikuti azitha kuzindikira bwino za ufuluwu ndi kukhalanso ndi mwayi ochitanawo zinthu zosiyansiyan pamoyo wao ngati anyamata.

Boma lanu linasayinira pangano loti lidzathandiza ndi kuonetsetsa kuti ana ndi achinyamata ali ndi ufulu wolandira ndi kupeza mauthenga ndi maphunziro okhudza umunthu, kugonana ndi ubereki. Linasayinira pangano loti zipangizo ndi zida zomwe achinyamata atha kugwritsa ntchito pankhani zogonana ndi ubereki zikupezeka mosavuta.

Komabe kafukufuku yemwe adachita a nthambi la bungwe la United Nations a UNICEF, UNFPA ndi UNESCO waonetsa poyera kuti izi zikichitika. Pakali pano ana andi achinyamata ambiri sakuphunzitsidwa pa nkhani za umunthu, kugonana, ubereki, makondomu, njira zolerera, zakusiyana pakagwiridwe kantchito pakati pa amuna ndi akazi, za ufulu wa chibadwidwe komanso ziphunzitos zina zolakwika.

"Maphunziro ndi chida chokhacho chimene chingagwiritsidwe ntchito posintha dziko lonse la pansi"

-Nelson Mandela, Pulezidenti

Udindo wanga ndi wotani ngati mtsogoleri wa ndale?

Thandizani ndi kuonetsetsa kuti ndondomeko zonse zomwe boma linakonza kuti lichite pankhani za maphunziro oyenera komanso okwanira okhudzana ndi za umunthu, kugonana ndi ubereki kwa achinyamata zikuchitikadi. Onetsetsani kuti inuyo panokha mwawerenga bwinobwino ndi kudziwa kuti ndondomekozi zikuti chiani. Onetsetsani kuti mwakonza ndondomeko ya ntchito imene muchite kuder kwanuko. Onetsetsaninsu kuti mwapeza ndalama zongwirira ntchito imeneyi.

Thandizani achinyamata kupeza mauthenga, mankhwala komanso thandizo lina lililonse lokhudza za umoyo - Nkhani zokhudza kugonana ndi ubereki pakati pa achinyamata sizikhalira okhao amene amachita mchitidwe ogonana ayi. Zimaimira wina aliyense popeza zimapereka upungu za m'mene munthu angadziletsere kuti asamachite zogonana, zam'mene angapezere ndi kukhalira ndi chibwezi chodaliliika choti nkumanganacho banja. Ndipo mauthenga omwe amaperekedwa kuchokera kwa alangizi achipatala ndi ofunika kwambiri kwa achinyamata.

Atsogoleri ali ndi udindo oteteza munthu aliyense - Ndi udindo wanu ngati mtsogoleri wa ndale kuonetsetsa kuti ufulu wa ana ndi achinyamata sukuphwanidwa. Onetsetsani kuti akuphunzitsidwa bwino pazonse zokhudza moyo wao ndi cholinga choti akhale athanzi komanso othandiza pachitukuko. Ngati mtsogoleri wandale khalani oyamba kutsogolera anthu kukambapo zakufunika kolangiza achinyamata kuipa koyamba kugonana akadali ang'ono. Athandizeni chonde.

Onetsetsa kuti ndondomeko zonse zomwe boma linasayinira ndi kukonza kuti lizichita malinga ndi African Youth Charter (AYC) ya mchaka cha 2006) potengeranso masomphenya a bungwe la African Union yotukula miyoyo wa ana ndi Achinyamata ikutsatidwa.

Ngati mtsogoleri wandle ndiye ndichite chiani kuti ndithandizepo?

- Ndikuthaniza ndi kuonetsetsa kuti ndondomeko zonse zomwe boma linakonza kuti lichite pankhani za maphunziro oyenera komanso okwanira okhudzana ndi za umunthu, kugonana ndi ubereki kwa achinyamata zikuchitikadi ndi kuunikidwa pafupipafupi. Ndi udindo wanga kuonetsetsa kuti ana asukulu ndi omwe sali pasukulu akulandira ndi kuphunzitsidwa bwino pankahni zimenezi. Ndi udindo wanganso kuonetsetsa kuti anthu akudera langa akutenga nawo mbali popereka maganizo awao ndi kuchita nawo zonse zokhudza ndondomekozi. Ndiponso ndi udindo wanga kuonetsetsa kuti ndalama ndi zipangizo zogwirira ntchitoyi zilipo.
- Auzeni ndi kukambirana ndi anthu anu za ndondomeko zonse zomwe boma linalonjeza kuti lizichita ndipo muonetsetse kuti zikuchitikadi. Yesetsani kuti zinthu zisinthe.
- Osakhala chete pankhani zophunzitsa achinyamata. Ngati atsogoleri a ndale auzeni ana ndi achinyamata za kuipa kwa miyambo ina monga kuchotsa fumbi, chokolo, kuchita mdulidwe pogwiritsa ntchito lezala limodzi, kulola kuti ana azikwatiwa kapena kukwatira akadali ang'ono, kukakamiza ana kukwatiwa kapena kukwatira, kukakamiza atsikana kuwayeza ngati adagonapo ndi mamuna kapena ayi pamoyo wao, kapena kusala anthu omwe adapezeka ndi HIV kapena olumala.
- Kopani mabungwe oti adzayambitse ntchito yophunzitsa anthu kudera lanu maphunziro oyenera komanso okwanira okhudzana ndi za umunthu, kugonana ndi ubereki ndi omwe angapangitse achinyamata kukhala odzidalira, otha kupanga zisankho pamoyo wao watsikunditsiku okhudza zogonana, komanso kudziletsa pankhani zogonana. Kuonjezera apa pezani ndalama ndi zipangizo zina zoti zithandize panchitoyi.
- Yambani kupereka uphungu mogwirizana ndi aphunzitsi a sukulu zoyandikana nazo komanso azachipatala kuti azidzapereka kwa achinyamata anu panthawi yomwe akuchita kalasi tsiku la Mulungu, kapana ku Madrassa, paubatizo ngakhalenso nthawi ina iliyonse yomwe pangapezeke mpata.
- Limbikitsani magulu onse omwe akugwira kale ntchitoyi mdera lanu ndipo mwatenge magulu amanewa ngati zitsanzo zoti ena amphunzireko. Mabungwe ndi magulu amenewa akhale “madolo” pazimani.

Ana ndi achinyamata ozindikira: Amapanga zisankho zabwino pamoyo wao: Mukhonza kukhala in oyamba!



SafAIDS Regional, Zimbabwe:

17 Beveridge, Avondale, P.O. Box A509, Avondale, Harare, Zimbabwe.

Tel: +263 4 336 193/4, Fax: +263 4 336 195

Website: www.saf aids.net